

Maphunziro
a
Alangizi othandizira
alimi a ziweto m'midzi

Zigawo za
thupi la ziweto


Small Scale Livestock and Livelihoods Program
PO Box 1604, Lilongwe Malawi





Zigawo za thupi la ziweto

Thupi la nyama

- Thupi la nyama ndilopangidwa ndi tinthu tating'onoting'ono tomwe pachingerezi amatitchula kuti tima cell. Tima cell timeneti ndi tamitundu yosiyanasiyana. Pali ma cell amene amapanga minofu, ma cell ena amapanga khungu/chikopa, ena amapanga mafupa, ena amapanga magazi.
- Tikamati thupi ndiye kuti ndilopangidwa ndi ziwalo zosiyanasiyana. Chiwalo ndi chigawo china cha m'thupi ndipo chimakhala ndi ntchito yakeyake. Mwa chitsanzo, impsyo imasefa magazi, mtima umapopa magazi, diso timaonera.
- M'thupi ndi m'mene zigawo zantchito zosiyanasiyana zimachitika. Ntchito zimenezi zimathandiza mosiyanasiyana ndipo zimatengera ziwalo zosiyanasiyana kuti zichitike.



Zigawo za ntchito za m'thupi:

Chigawo	Ntchito yake
Chogaya zakudya	<p>Chimathandiza kutenga zakudya kupititsa m'thupi kuti ligwiritse ntchito zosiyanasiyana</p> 
Chopumira	<p>Kulowetsa mpweya wabwino kuti thupi lipeza mphamvu</p> 
Chopopa magari	Kupopa magari ku ziwalo zonse kuti thupi likhale ndi moyo
Choganiza	Kuteteza minofu ndi ziwalo.
Chaminofu ndi mafupa	Kuti thupi liziyenda pogwiritsa ntchito minofu ndi mafupa
Chamkodzo	Chimasefa magari kuchotsamo zosafunika ngati mkodzo
Choteteza kumatenda	Chimagonjetsa matenda.

- Tiyeni tione mozama pang'ono za zina za ziwalo zofunika zedi m'thupi.

Ziwalo m'thupi:

Chiwalo	Ntchito yake
Chifu	Chimagaya zakudya powiritsa ntchito madzi ogayira ndi kuchipanga phalaphala limene limatsikira kumatumbo
Matumbo	Matumbo amayamwa zakudya zoyenera kutumiza m'thupi ndipo zosayanera zimaturuka ngati manyi, ndowe kapena zitosi.
Chiwindi	Chiwindi chimasefa magari ndi kuchotsa ma cell akufa wonse. Chiwindi chimapanga madzi a ndulu omwe amathandizira pogaya zakudya m'mimba. Ngati chiwindi chilephera kugwira ntchito, nyama imadwala ndi kufa, Pali matenda ena omwe amachititsa kuti chiwindi chisagwire ntchito yake bwino. Pali tizirombo tina tomwe timalowa m'thupi ndikumakakhala mchiwindi.
Impsyo	Imasefa magari ndi kutaya zoipa ngati mkodzo Pali matenda ena omwe amachititsa kuti magari abzyole sefa muimpso ndi kukasakanizika ndi mkodzo, ndipo nyama imakodza mkodzo wofiira.
Mapapo	Mapapo amatenga mpweya wabwino ku upititsa m'magazi. Amachotsanso mpweya woyipa kuchokera m'magazi. Mpweya umalowa ndi kutuluka m'mapapo kudzera mu nkhwiko.
Magazi	Magazi amagawa mpweya wabwino ndi zakudya zogayagaya ku ziwalo zonse za m'thupi kuti zigwire bwino ntchito yake. Amatenganso zoipa zotha ntchito kuchokera ku ziwalo za m'thupi kukazitaya kudzera kuziwalo zosiyanasiyana monga impyso.
Mtima	Umapopa magari m'thupi lonse. Ukamagunda mtima, ndiye kuti uli kupopa magari
Mitsempha yotenga magari kuchokera ku mtima	Iyi ndi mitsempha yomwe imatenga magari kuchokera mumtima kupita ku ziwalo zonse za m'thupi. Magazi nthawi zonse amakhala ndi kuyenda m'mitsempha. Mitsempha ina ndi yaying'ono kwambiri. Magazi sayenera kutuluka m'mitsempha. Pathupi pamatupa ngati magari atuluka pamene pavulazidwa.
Mitsempha yobweretsa magari ku mtima	Iyi ndi mitsempha yomwe imabweretsa magari kumtima

Chiwalo	Ntchito yake
Bongo	<p>Bongo umaongolera zonse zochitika m'thupi. Umaongoleranso zochita za minofu.</p> <p>Matenda okhundza bongo amapangitsa chiweto kumakomoka ndi kumangozungulira apo chakhala.</p> <p>Bongo umaongolera zinthu ngati izi, kumva, kusachita chizungulire, kuona, fungo, kumva kukoma kapena kuwawa ndi kumva kukhudzidwa pathupi</p>
Ma nerve	<p>Awa amagwira ntchito ngati mawaya amagetsi ndi kumayendetsa ntchito za minofu. Mitsempha imanyamula uthenga pakati pa ziwalo ndi bongo.</p>
Lymph nodes, Kapamba, mafuta a m'mafupa	<p>Awa ndi asilikali omenyana ndi matenda m'thupi.</p> <p>Matenda ena amapangitsa kuti mwana bere a zitupa. Akatupa timati mwana bere.</p> <p>Zakudya zabwino zimapangitsa kuti ziwalo izi zigwire bwino ntchito yogonjetsa matenda.</p>

Yankhani mafunso awa:

Gulani chiweto ndipo muchiphe ndi kuchiganga bwinobwino. Tazindikirani ziwalo zimene tanena m'mwambazi.

Apa mutha kuonanso chiwetocho chikuonetsa zizindikiro za matenda musanaphe ngati zilipo. Muthanso kuona zizindikiro zamatenda kuziwalo za nyama yomwe mwaigangayo.

Mafunso apomaliza pa maphunziro a gawo

1. Tchulani zina mwa zigawo zantchito za m'thupi la nyama
2. Kodi ziwalo izi ntchito yake ndi chiyani m'thupi la nyama?
 - Matumbo
 - Chiwindi
 - Impsyo
 - Mapapo
 - Mtima
 - Magazi